Kusanthura (Kumasulira) Baibulo (Bible Interpretation)

Akristu onse amagwirizana kuti Baibulo ndi Mau a Mulungu. Amakhulupilira kuti Mulungu amalakhura nafe momveka ndipo Baibulo siritsutsana pamamasulidwe ake. Liri ndi tanthauzo lenileni limene Mulungu anali nalo pouzira Mau ake kwa anthu amene ankalemba Baibulo. Gawo lina la Baibulo likhoza kukhala ndi malongosoledwe ena komatu tanthauzo lake ndi limodzi, ndipo iri ndi tanthauzo lomwe wolemba kupyolera pakuwuziridwa ndi Mzimu Woyera anali nalo.

Cholinga chomasulira Baibulo ndi kuti tipeze tanthauzo lenileni la wolemba kuti timvetsetse bwino. Mavuto amene timakhala nawo popeza tanthauzo amachitika chifukwa cha chiyankhulo, nthawi yomwe zinthuzo zinkachitikira ndi kusiyana kwa chikhalidwe kwa pakati pathu ndi anthu amene uthengawo ankaulandira pachiyambi.

Nanga tingadziwe bwanji tanthauzo lenileni la Mau a Mulungu? Mzeru zozama za kumasulira Baibulo zimafunafuna kupeza njira zomasulira Baibulo molondora bwino. Kamasulidwe kabwino kamapereka njira zothandizira kutsimikizira kuti tikudalira kumasulira kwathu kwa Baibulo pa choonadi chochokera ku Mau a Mulungu.

Pogwiritsa ntchito mfundo zomveka bwino zakumasulira Baibulo chofunika kwambiri ndi kurimvetsetsa Baibulo. Paulo ntumwi amatifotokozera kuti “uchite changu kudzionetsera kwa Mulungu wobvomerezeka, wa ntchito wopanda chifukwa cha kuchita manyazi wolunjika nao bwino mau a choonadi” 2 Timoteo 2:15).

Cholinga cha phunziroli ndikufotokoza mwachidule mfundo zakamasuliridwe ka Baibulo.

I. Zomwe muyenera kukumbukira za Baibulo

1. Kumvetsetsa kapena kumasulira Baibulo

A. Petro ntumwi anakumbutsa awerengi ake kuti zinthu zina zolembedwa ndi Paulo zinali zovuta kuzimvetsetsa (2 Petro 3:15-16).

B. Ziripo ndime zina m’Baibulo zomwe zimakhala zovuta kuzimvetsetsa. Chitsanzo chandime ngati zimenezi ndi Genesis 6:2. Sitidziwa kuti ana a Mulungu anali ndani. Deutronomo 29:29 ndi Yesaya 55:8-9 akutiphunzitsa kuti Mulungu sanaulure chirichonse kwa ife anthu; ndipo kuti malingaliro ake ndi osiyana ndi ife. Chinthu china chomwe sitichimvetsetsa chikupezeka pa Exsodo 28:30 ndipo chimalankhula za *Urimu* ndi *Tumimu*. Timaona mau amanewa malo osiyanasiyana m’Chipangano Chakale koma sitidziwa chomwe amatanthauza.

C. Zinthu zomwe ife sitimazimvetsetsa sizofunikira kwenikweni. Zinthu zonse zofunikira m’Baibulo ndizosavuta kuzimvetsetsa ndipo zimabwerezedwa kawirikawiri potsimikira.

i. Aliyense akhoza kumva magawo a Baibulo ngakhale osakhulupilira. Komabe magawo ambiri a Baibulo sangamveke kwa osakhulupilira. Chifukwa chake m'chakuti Mzimu Woyera umathandizira ife kumvetsetsa zomwe Mau a Mulungu akutanthauza ndi m'mene tingawatanthauzire (1 Akolinto 2:14). Mwanjira ina timafuna mphamvu ya Mzimu Woyera kutithandizira kumvetsetsa zozama zake za Baibulo. Ndikufuna kubwerezanso kuti, Osakhulupilira sangamvetsetse za Baibulo chifukwa Mzimu Woyera umafunikira kuti amvetsetse bwino ndipo ndi akhristu okha amene ali ndi Mzimu Woyera.

2. Mulungu anauzira Baibulo

A. Ndi ntchito ya Mulungu (2 Timoteyo 3:16) ndiponso cholinga cha Mulungu kuti Baibulo lilembedwe. Anthu analakhura ndipo Baibulo linalembedwa motsogozedwa ndi Mzimu Woyera (2 Petro 1:20-21).

B. Akhristu timakhulupilira kuti Baibulo ndi choonadi cha Mulungu, liri ndi ulamuliro ndipo liribe cholakwika china chirichonse ndipo ndi lokwanira pa chiphunzitso.

C. Baibulo ndi Mau enineni a Mulungu. Inde, anthu analemba Baibulo, ndipo ankalemba m'chiyankhulo chao ndi m'njira zao. Komatu ankalankhura molangizidwa ndi Mzimu Woyera.

i. Izi zikutanthauza kuti ankalankhura Mau a Mulungu. Zomwe ankalankhura sizinali za m'maganizo awo. Iwo sanali eni ake a choonadi chomwe chinkalankhuridwacho; iwo anali njira chabe. Choonadichi chinali cha Mulungu mwini. Tanthauzo lake linali lochokera kwa Mulungu. Mulungu ankalankhura uthenga wake kupyolera mwa wolemba Baibulo.

ii. Sikuti anangolemba kokha zochokera kwa Mulungu, komatu zomwe iwo ankalemba zinali zolamulidwa ndi Mzimu Woyera. Mulungu sanangovumbulutsa choonadi kwa wolemba Mau a Mulungu ndi kungowasiya kuti afotokozere molondora. Petro akuti pamene iwo anali kufotokozera anali kutsogozedwa ndi Mzimu Woyera. Kulemba kwa Baibulo sikunasiyidwe m'manja mwa anthu; komatu Mzimu Woyera unatsogolera mpaka pa mapeto (2 Petro 1:21).

iii. Izitu sizikutanthauza kuti Mulungu anafotokozera mau alionse. Komatu Mzimu unali m'mitima yawo ndipo wolemba ankasankha ndi kulemba mau, maganizo ndi mzeru zao zomwe zinkapereka uthenga wa Mulungu molondora bwino. Choncho mau a wanthu wolemba Mau a Mulungu ndi Mau a Mulungu ndithu.

iv. Paulo akutiphunzitsa kuti Mau onse anauziridwa ndipo amapindulitsa m'chiphunzitso 2 (Timoteo 3:16). Baibulo lonse Chipangano Chakale ndi Chatsopano ndi choonadi chochokera kwa Mulungu ndipo motsogozedwa ndi Mzimu Woyera, anali kulemba mauwo.

3. M'Baibulo mulibe cholakwika chirichonse.

A. Muzolembedwa zoyambilira mulibe cholakwika china chirichonse.

B. Mabaibulo athu amakono muli zosiyana zina, komabe tanthauzo lenileni la Baibulo sirinasinthe. Mulungu amateteza uthenga wa Baibulo, komatu sanapereke zozizitswa kuti olembawo asalakwitse posamutsira zolembedwazo ku mabuku ena. Zolakwika zimene osamutsira zolembedwa zakale ku mabuku amapanga sizofunikira. Taonani ndime izi za Baibulo (2 Samueli 10:18) akuti okwera kavalo mazana asanu and awiri (700) koma 1 Mbiri 19:18 akuti zikwi zisanu ndi ziwiri (7000). 2 Mafumu akuti mfumuyo inali ndi zaka khumi zisanu ndi zitatu (18) ndipo (2 Mbiri 36:9) akuti anali ndi zaka zisanu ndi zitatu (8). Tikuona kuti 1 Mafumu 4:26 ndi 2 Mbiri 9:25 akusiyana pa chiwerengero cha akavalo.

C. Mabaibulo abwino monga KJV, ESV ndi NASB ndi okhawo amene amapereka matanthauzo abwino. Mabaibulo amakono a ESV ndi NASB amapangidwa mogwirizana kwambiri ndi zolembedwa zakale zoyambilira zomwe zikupezekabe lero lino; pakupereka matanthauzo mogwirizana kwambiri ndi zolembedwazi.

D. Chonde musamawerenge mabaibulo abodza monga a Mboni za Yehova (NWT) komanso a Chimomoni.

E. Simuyeneranso kuwerenga mabaibulo atsopano kwambiri a NIV chifukwa anasintha zinthu zambiri monga malo ambiri pamane panayenera kukhala “iye” anayikapo “iwo.” Mukhoza kuwadziwa mabaibulowa poyang’ana zizindikiro za malamulo a kope rayiti (Copy right) monga NIV yemwe anachita kope rayiti m’chaka cha 1984 mukhoza kugwiritsira ntchito.

4. Umodzi wa Baibulo. M’Baibulo muli mabuku okwanira makumi asanu ndi limodzi mphambu zisanu ndi chimodzi (66) ndipo linalembedwa ndi alembi okwana makumi anayi osiyanasiyana pamaphunziro awo, kwa zaka zokwana chikwi ndi mazana asanu ndi chimodzi (1600). Izi zinali chomwechi chifukwa Mulungu mwini anathandizira kulemba Baibulo.

5. Baibulo lonse likupereka uthenga wa Khristu Yesu. Chipangano Chakale chonse chimafotokoza za chiyembekezo cha kubwera kwa Khristu ndipo Chipangano Chatsopano chimayang’ana m’mbuyo za kubwera kwa Khristu. Kumasulira Baibulo kumakhala ndi malamulo, mfundo, ndi njira zotanthauzira Baibulo. Pamakhala dongosolo loyesetsa kumvetsetsa tanthauzo lenileni la ndime za m’Baibulo pofuna kupeza chomwe ndimezo zikutanthauza lero lino.

A. Cholinga chenicheni ndi kupeza tanthauzo la wolemba kwa anthu omwe mlembiyo ankawalembera ndikupezanso tanthauzo lomwe ndimeyi ikufotokoza lero lino. Malamulo ena a m’Chipangano Chakale sakugwira ntchito lero lino monga a zakudya ngati nkhumba ndi zina zotero.

6. Baibulo liri ndi ulamuliro wonse

A. Baibulo ndi lochokera kwa Mulungu; ndipo tiyenera kumvera zonse zolembedwa m’menemo.

II. M’chifukwa chiyani Baibulo liyenera kumasuliridwa?

1. Kumasulira ndi kwabwino kwambiri chifukwa sitikhala munthawi ndi chikhalidwe cha omwe ankalembawo. Zoona ndi zakuti wolemba Baibulo sali ngati anthu amene ayima mbali ina ya mtsinje ndipo ife tiri mbali ina ya mtsinje. Kumasulira Baibulo ndi njira yomwe timalumikizira mtsinje ndi cholinga chakuti uthenga weniweni wa Baibulo ukathe kuoloka mtsinje; kwa ife kuti timvetsetse uthenga weniweni wa pachiyambi. Pali zinthu zina zomwe anthu a m’Baibulo ankazimvetsetsa, komatu ngakhale titagwiritsa ntchito malamulo onse omasulira Baibulo timalepherabe matanthauzo ena. Mwachitsanzo sitimvetsetsa matanthauzo a *Urimu* ndi *Tumimu* ngakhale anthu a m’Baibulo ankadziwa matanthauzo ake (Exodo 28:30) ndi (Numeri 27:21). Zinthu zonse zomwe sitimvetsetsa sizofunika kwambiri pa chiphunzitso cha Baibulo.

B. Chenjerani ndi anthu amene amanena kuti amadziwa lemba lirilonse la m’Baibulo.

III. Njira zosiyanasiyana za kamasulidwe

1. Kufunika kwa kuonetsetsa. Ganizirani (Luka 17:21) “taonani ufumu wa Mulungu uli pakati panu.”

A. Yang’anitsitsani pa ndimeyi ndipo funsani ndi kuyankha mafunso otsatatirawa:

i. *Kodi akulankhurayo ndi ndani? Yesu ndi amene akulankhura.*
ii. *M’chifukwa chiyani amalankhura? Ankayankha funso.*
iii. *Mfunso lanji? Kodi ufumu wakumwamba ufika liti?*
iv. *Ndani anafunsa funsoli? Afarisi.*
v. *Afarisi anali ndani? Lina gulu la chipembedzo lomwe linkatsutsana ndi Yesu.*
vi. *Nanga Yesu anali ndani? Anali Mwana wa Mulnugu, Mesiya. Ndi mfumu ya Ufumuwo.*

B. Pogwiritsa mafunsowa komanso zina, tikhoza kumasulira ndimeyi. Tikudziwa kuti Afarisi sanali Akhristu ndipo tikudziwa kuti Ufumuwo sunali pakati pawo. Tikudziwa kuti Yesu ndi Mfumu ya Ufumuwo kotero zikutanthauza kuti kupezeka kwa Yesu, Ufumu wa Mulungu unali pakati pao.

C. Kugwiritsa ntchito malamulo achiyankhulo nkofunuka kwambiri. Asaduki sankakhulupilira za kuuka kwa akufa. Yesu anati (Mateyu 22:29-32), Iye sanali Mulungu wa akufa. Akugwiritsa ntchito mau oti “sali” m’malo mwa “sanali” kutsimikiza kuti Abrahamu, Isaki ndi Yakobo alipobe ndi moyo.

D. Muyenera kukhala ndi nthawi yokwanira komanso kusikhasikha pandime yomwe mukuifuna. Werengani ndimeyi kambirimbiri.

E. Onani chitsanzo chotsatirachi: Yohani 5:24 “Indetu, indetu, ndinena kwa inu, kuti iye wakumva mau anga, ndi kukhulupilira Iye amene ananditumа Ine, ali ndi nao moyo wosatha, ndipo salowa m’kuweruza koma wachokera kuimfa, nalowa m’moyo.”

i. *Kodi mau ofunikira kwambiri ndi ati? Ndi “indetu,” “moyo wosatha” “kuweruza” ndi “imfa.”*

ii. *Kodi mau amenewa akulumukizana bwanji? Yesu akugwiritsa ntchito mauwa kulumikiza imfa ndi moyo.*
iii. *Akulankhulayo ndi ndani? Yesu akulankhula.*
iv. *Kodi Yesu akulankhura ndi ndani? Akulankhura ndi Ayuda.*
v. *Kodi Ayuda anayilandira bwanji nkhaniyi? Ayuda anakwiya nafuna kupha Iye.*
vi. *Kodi malamulo achiyankhulo akugwiritsidwa bwanji? Zikutanthauza kuti munthu akangokhulupilira amalowa m'moyo wosatha.*

F. Kumasulira kolondora ndi uku; Yesu anali ndi phunziro lalikulu loti anthu amve. Akuti moyo wosatha sichinthu chimene munthu amachipeza mtsogolo; ndi chinthu chimene munthu amachipeza tsopano. Kufunika kwa vesi limeneli ndi kwakuti akulankhula zakusiyana kwa imfa yosantha ndi moyo wosantha. Akuti okhulupilira amakhululukidwa ku machimo ake ndipo adzakhala ndi Yesu kumwamba kunthawi zosantha.

2. Ndani analemba/analankhula m'ndimeyi ndipo ankalankhula kwa ndani? Nanga tikuphunzira chiyani pa ndimeyi?

A. Ndikofunika kwambiri kumvetsetsa wolemba pa ndime yomwe yasakhidwa, kuti iye anali ndani, khalidwe la nthawi imeneyo limene linapangitsa kuti alembe ndimeyi. Chofunika kwambiri ndikudziwa cholinga cholembera buku. Mwachitsanzo, Yohani 20:31 akufotkoza cholinga cholembera Uthenga Wabwino, "koma zalembedwa izi kuti mukakhulupilire kuti Yesu ndiye Khristu Mwana wa Mulungu, ndi kuti pakukhulupilira mukhale nao moyo m'dzina lache." Yohani akufotokoza cholinga chake pa uthenga wabwino, komatu nthawi zambiri kumakhala kovuta kupeza cholingachi. Njira izi zingakuthandizeni kupeza cholinga cha wolemba ndi chikonzero chimene anali nacho.
B. Yambani kufufuza ngati cholinga cha wolemba chafotokozedwa kapena ai. Ndipo ngati sichinafotokozedwe, ngati pali zinthu zina zomwe zikusonyeza za cholingachi. Palibe m'makalata onse a Paulo ku Akolinto pomwe akufotokoza za cholinga, koma tikhoza kupeza za cholingachi tikawerenga 1 Akolinto 1:11, 3:3 & 4, 4:6, 5:6 etc. Tikawerenga ndime zimenezi tikupeza kuti kunali mavuto ambiri mu mpingowu. Anthuwa ankalimbana kwambiri ndi undindo ndi ulamuliro wa Paulo ntumwi. Paulo analemba kalatayi pofuna kukonzetsa mavutowa. Muyenera kukhala ngati wa Polisi wa zofufuzafuza ndipo pezani njira zoti zikuthandizeni kumvetsa nkhaniyi.
C. Maumboni a awerengi amasonyeza cholinga cha buku. Mitu ya maphunziro yomwe yabwerezedwa imasonyeza chikonzero ndi cholinga cha mlembi.
D. Yang'ani zigawo za buku. Mabuku ambiri ali ndi machaputala.
E. Pamene cholinga kapena chikonzero chamveka bwino werengani magawo a buku ndi cholinga ndi chitsimikizo chakuti kumasulira kwanu kukugwirizana ndi ndimeyi. Chitsanzo chabwino ndi Afilipi 2:1-8. Ndimeyi ikusonyeza cholinga cha mlembi. Mau oti "ndi mtima umodzi, chikondi chimodzi pogwirizana" zikusonyeza kuti Paulo anakhudzidwa ndi chiyanjano cha Akhristu aku Afilipi ndipo mavesi 5-8 akuwakumbutsa chitsanzo cha Khristu. Khristu anali ndi mtima wina kotero ankachita zinthu mwanjira zodabwitsa.

2. Kodi ndime imeneyi ikunena chiyani m'mau omveka bwino?

1. Pamene mukuwerenga ndime ya m'Baibulo muyenera kudziwa kuti pamakhala kuyankhulana pakati pa wolemba Baibulo ndi inu ndipo Mulungu amakhala mwini weniweni wolemba. M'chifukwa chake owerenga ayenera kuchita kafukufuku wa tanthauzo la chomwe mwini mlembi (Mulungu) akutanthauza. Chomwe muyenera kudziwa m'chakuti pamakhala tanthauzo limodzi lokha la ndime.

2. Dziwani kuti ndime zambiri za Baibulo ndizosavuta kuzimvetsetsa, simuyenera kuzipanga kukhala zovuta.

3. Fufuzani mau okhala ndi tanthauzo lenileni ndipo muone kuti lero lino mauwo akutanthauza chiyani. Ntchito yathu yoyamba ndi kupeza chomwe wolembayo pachiyambi ankatanthauza mu ndimeyo. Ndipo kenako tiyenera kufanizitsa tanthauzo la nthawi imeyo ndi m'mene lero lino tikuwamvera mauwo.

   i. Mwachitsanzo pamene Paulo ankalemba Kalata ya Akolose ankalemba kalatayi chifukwa cha ziphunzitso zonyenga zimene zinali kumeneko nthawi imeneyi zomwe iye ankawachenjeza. Chifukwa cha ichi anagwiritsa mau ogwirizana ndi ziphunzitso zonyengazo komatu anawagwiritsa ntchito potanthauzira chinthu china. Chitsanzo chabwino ndi pamene Paulo akugwiritsa ntchito mau oti "chinsinsi chinabisika" Akolose 1:25-26. Mau amenewa ankagwiritsidwa ndi anthu aziphunzitso zonyenga kutanthauza kuti zinsinsi zobisika zodziwika kwa anthu ochepa okha. Koma Paulo akugwiritsa ntchito mauwa pofuna kutanthauza chikonzero cha Mulungu chachipulumutso chomwe sichinkadziwika kale koma tsopano chadziwika kwa aliyense kupyolera m'ntchito ya Yesu Khristu. Dzina la Yesu linali ngati lachinsinsi m'Chipangano Chakale koma tsopano tadziwa kuti ndi dzina lomwe tiyenera kupulumutsidwa nalo.

4. Tisanapeze tanthauzo lenileni la ndime kwa ife, tiyenera kufufuza ndimeyi poyang'ana mau (aneni[maverebu] ndi akapanda mneni[mafulezi]) kuti tione m'mene mauwo tingawagwiritsire nthito lero lino monga Levitiko 11:7.

   A. Kumbukirani kuti ziripo ndime ndi ziphunzitso zina zomwe sizingagwiritsidwe ntchito lero lino. Ndime zoterozi zimatchedwa *mthunzi* (zosinthika). Mwachitsazo, malamulo onse akapembedzedwe ka ana a Israeli monga malamulo a nsasa okumaniranako (kachisi), malamulo antchito ya ansembe, malamulo operekera nsembe sakugwira ntchito kwa ife lero lino chifukwa zinali kungolosera zakubwera kwa Khristu.

   B. Nthawi zina mau a m'Baibulo akhoza kugwira ntchito kwa ife m'njira zina. Mwachitsanzo pamene Paulo akupempha mpingo kupatsana moni (malonje) ndi mpsompsono wa chikondi (1 Petro 5:16). Lero lino tikhoza kunena kuti kulonjerana mwachikondi pogwirana dzanja.

   i. Ndikofunika kwambiri kupeza mau (aneni ndi akapanda mneni) omwe ankagwira ntchito pa nthawi ya kalelo komanso tsopano popanda kusintha kuli konse. Tikatero timati *zinthu zosasinthika.* Mwachitsanzo zinthu zosasinthika ndi monga, Mulungu

akuletsa m'chitidwe wa *mathanyura* (Aroma 1:27). *Mathanyura* linali tchimo m'Chipangano chakale komanso lero lino nthawi ya Chipangano Chatsopano.

ii. Sitiyenera kutenga *mthunzi* monga *zinthu zosasinthika* chifukwa izi zimapanga ife kukhala alamulo (Afarisi). Mwachitsanzo Yesu anasambitsa mapazi ophunzira ake. Ifetu sitikuwuzidwa kuti tidzisambitsana mapazi lero lino.

C. Kodi chinthu chomwe chikuchitika m'ndimeyi ndi chiyani? Tikati "zochitika" zikutanthauza nthawi, malo ndi m'mene mauwo akugwiritsidwira ntchito. Mau ambiri, a Chingerezi ali ndi matanthauzo osiyanaosiyana potengera m'mene mauwo akugwilira ntchito.

5. Pezani mathero anu pamene mwawerenga.

A. Kodi mathero anga ndi ati pa ndime imeneyi? Nanga ndikumva chiyani pandime yomwe ndawerengayi?
B. Kodi anthu ena anamasulira bwanji ndimwe yomweyi? Apa muyenera kuwerenga mabuku ena. Koma chenjerani ndi zomasulira za anthu ena chifukwa mukhoza kupezeka zolakwika zina. Kodi mathero aulaliki wanga akugwirizana kapena kutsutsana ndi ndime ya Mau a Mulungu ndasankhayo ndi anthu ena omwe anawerenga ndi kumasulira ndime yomweyi?
C. Nanga ine ndaphunzira chiyani ndipo ndingathe kugwiritsa bwanji zinthu zomwezi m'moyo wanga?
D. Kumbukirani mulibe zolakwika ziri zonse m'Baibulo. Ndipo ngati mwapeza cholakwika kapena chotsutsana m'Baibulo fufuzani chifukwa dziwani kuti cholakwikacho kapena chotsutsanacho chiri ndi inu osati Baibulo.

6. Kufunika kolalikira moyang'ana nthawi, malo ndi zomwe zikuchitika. Nthawi zambiri nthawi, malo ndi zomwe zikuchitika zimathandizira kupeza tanthauzo la mau kapena ndime. Tikati kulalikira koyang'ana nthawi, malo ndi zomwe zikuchika tikutanthauza njira ya m'mene mauwo agwiritsidwira ntchito.

A. Machitsanzo mau oti kuthamanga. Mwana akuthamanga kusukulu. Bambo Zatopetsa akuthamanga magazi pa nkhaniyi. Apa tikuwona kuti mau oti "akuthamanga" ali ndi matanthauzo awiri malingana ndi m'mene mauwo akugwiritsidwira ntchito.
B. Chitsanzo china ndi mau oti *kugona* m'Baibulo. Amatanthauza kuguna tulo pa Mateyu 28:13. Mau omwewo akutanthauza imfa pa 1 Atesolonika 4:14.

7. Pali *nthawi, malo ndi zomwe zikuchitika* magawo awiri zomwe tiyenera kuziganizira pamene tikumasulira Baibulo: *Nthawi, malo omwe zinthuzo zinachitika* ndi tanthauzo *wamba kapena chomwe chikuchitika* pa nthawiyo.

A. Nthawi, malo komwe zinthuzo zinachitika
Ndikofunikira kwambiri kumvetsetsa zachomwe chinkachitika pa nthawi yomwe wolemba ankalemba ndime ya m'Baibulo kuti timvetsetse tanthauzo la ndimeyo.

i. Chitsanzo chabwino ndi nkhani ya Msamariya wa chifundo mu uthenga wabwino omwe ukupezeka m'buku la Luka (10:25-37). Tikudziwa kuti Ayuda ankadana ndi Asamariya. Ankawada chifukwa Ayuda a chigawo cha Kumpoto cha Ufumu wa Israyeli atachotsedwa m'dziko lawo ndi Asuri, Asamariya anapatsidwa dzikoli lomwe linali la Ayuda. Kotero nkhani imeneyi iri ndi tanthauzo lina lapadera. Iri ndi phunziro lotiphunzitsa chikondi pakati pathu lomwe Baibulo tikutiuza kuti tidzikhala nalo pa anzathu Pamene tikuwerenga nkhani imeneyi m'buku la Luka, tikuona kuti Ayuda awiri a chipembedzo sanafune kusamala wapaulendo wovulazidwa uja, koma Msamariya wonyozedwa uja ndi Ayuda, anathandiza wovulala uja kwambiri. Kodi m'nkhani imeneyi ndi ndani anasonyeza kuopa Mulungu?

Tsopano tikuona mbiri ya m'mene zinthu zinaliri, kenako tiyenera kuona chomwe chikupangika. Nanga phunziro lomwe tikuphunzira ndi liti lero lino? Phunziro lomwe tikuphunzira lero lino ndi lakuti tiyenera kukonda anzathu komanso kukonda anthu ena ngakhale atakhala a mtundu wina (tsankho pakati pa akhristu silofunika).

B. Pa zomwe zikuchitika kapena zomwe mau akufotokoza. Chomwe chikunenedwa kapena kuchitika chimapereka tanthauzo lapadera la ndime. Kotero tikhoza kusintha tanthauzo la mau ngati titapanda kuganizira chochitikacho. Munthu yemwe akufuna kukwatira akhoza kugwiritsa ntchito mau omwewa molakwika posaganizira pa zochitika ndi mbiri, kutsimikizira kuti akufuna kukwatira mwansanga. Mwachitsanzo:

i. Gawo lomaliza la 1 Akolinto 7:36 "akwatitsidwe kapena akwatire."

ii. Yohani 13:27 akuti "chimene uchita chita msanga."

iii. Kotero simungatenge ndime ziwiri ngati zimenezi ngati zokuthangatirani kufuna kukwatira mwachangu. Palibe m'gwirizano ulionse pa mavesi amenewa.

C. Poyamba yambani kuyang'anitsitsa pachomwe chikuchitika ndi zomwe zikutanthauza; onani kodi mavesi omwe ayandikizana nao akuti chiyani kuti mupeze tanthauzo lenileni la vesi yomwe mukufuna kuyimvetsetsa.
D. Kuopsa kwa kusayang'ana chomwe chikuchitika kapena chikunenedwa. Mukhoza kupanga Baibulo kulankhula chirichonse mukuchifuna komwe kuri kulakwitsa. Izi ndi zimene magulu abodza amachita popanga ziphunzitso zao zonyenga.

E. Kusafuna kuyang'ana zomwe zikunenedwa ndikuchitika kumapangitsa kamasulira molakwika vesi. Tiyeni tione zitsanzo ziwiri:

i. Nthawi zina anthu amagwiritsa ntchito vesi limodzi kunja kwa zimene zikunenedwa pofuna kutsimikizira zomwe Baibulo sirikunena. Anthu amafuna kuti Baibulo linene zomwe iwo akufuna ndipo uku kamakhala kugwiritsa molakwika Mau a Mulungu.

ii. Mwachitsanzo, pamene anthu akufuna kufotokoza kuti kumwa vinyo nkolakwika amagwiritsa ntchito vesi la Luka 1:15 potsimikizira mfundo yawo. Uku nkulakwitsa chifukwa ndimeyi ikuyambira pa vesi 13 ndipo ndi gawo la uphungu ochokera kwa m'ngelo omwe udapatsidwa kwa atate ake a Yohani m'Batizi. Kotero kuti vesili sirikuletsa kumwa vinyo kulikonse. Palitu ndime zambiri za Baibulo zomwe zikhoza kugwiritsidwa ntchito kusamwa vinyo m'madera momwe ife timakhala makamaka m'madera momwe muli dzidakhwa (mbiya ng'ambe) zambiri (Aroma 14:13).

iii. Anthu ena amagwiritsa ntchito Luka 10:9 and 19 kutsimikizira kuti lero lino tikhoza kuchiritsa odwala ndipo kuti akhristu onse ali ndi mphamvu ya machiritso. Koma zoona ndi zakuti ndime ya Luka 10:1-19 yomwe ikuwonetsa kwa ife kuti Yesu anapereka mphamvu zapadera zimenezi kwa ophunzira aja makumi asanu ndi awiri ndi mphambu ziwiri (72) omwe iye anawatumiza. Sitikuwerenga kuti akhristu onse anapatsidwa mphamvu imeneyi.

iv. Zinthu zomwe tiyenera kuziganizira pamene tikumasulira Baibulo

1. Kodi wolemba bukulo anali otani? Nanga izi zikukhudza bwanji zolemba zake? Zolembedwa zambiri zimakhala ndi matanthauzo atsopano pamene zikuwerengedwa poona nyengo zomwe wolembayo ankalembera.

A. Chitsanzo chabwino ndi Masalimo 51 omwe Davide analemba atachimwa tchimo la chigololo ndi Betiseba zomwe zinapangitsa kuti Uriya mwamuna wa Betiseba aphedwe. Analemba Salimoli ndi mtima olapa pamene akulapa machimo ache ndipo akupempha kukhululukidwa. Chaputala ichi chikuphunzitsa kulapa koonadi.

2. Tiyenera kumvetsetsa mbiri ya Chipangano Chakale kuti timvetsetse Chipangano Chatsopano. Sitingamvetsetse buku la Aheberi pokhapokha titamvetsetsa Chipangano Chakale.

A. Yesu ankagwiritsa ndime zambiri za Chipangano Chakale pofuna kuphunzitsa mfundo zina. Kawirikawiri tikhoza kugwiritsa ntchito Chipangano Chakale kufotokozera ndime ya Chipangano Chatsopano. Mwachitsanzo, Yesu anagwiritsa ntchito Numeri 21:4-9 pamene anauza Nikodemo, "Monga Mose anakweza njoka m'chipululu, koteronso mwana wa munthu ayenera kukwezedwa." Pamene ife timvetsetsa mbiri ya Chipangano Chakale, timatha kuona chifanizo. Ayuda anauzidwa kuyang'ana kumwamba kuti akhululukidwe ndi kuomboledwa monganso timayang'ana kwa Yesu pa chikhululukiro cha machimo athu.

3. Zinthu zinanso monga Mbiri ndi mapu aderalo akhoza kuthandizira kumvetsetsa ndime ya m'Baibulo. Mwachitsanzo masomphenya a chifanizo chachikuru chomwe chiri m'buku la Danieli (Danieli 2:31-45), chomwe chinkayimira kuuka ndi kugwa kwa mafumu anayi a Babulo, Aperezi, AGiriki

and Aroma. Mabuku ena ambiri akhoza kutiphunzitsa zambiri za mafumuwa ndi kutithandiza ife kumvetsetsa zifukwa zomwe ansonkho monga ntumwi Mateyu anali odedwa kwambiri pakati pa Ayuda. Chifukwatu anthuwa anali a katangale ndi ziphuphu kwambiri.

A. Nthawi zinanso kudziwa mapu a deralo zimathandizira kumvetsesta ndime yosankhidwayo. Mwachitsanzo Yesu anayamba kufotokoza fanizo la Msamariya wa chifundo ndi kuti: “Munthu wina anali paulendo ochokera ku Yerusalemu kupita Yeriko….” (Luka 10:30). Izitu zingatithandizire kuzindikira kuti inali njira ya mapiri komwe nthawi zambiri kunkabisala mbava (akuba, zigawenga atsizina mtole, andipsi).
B. Kudziwatu miyambo ya anthuwo kumathandizira ndime monga (Aefeso 5:21-6:9), mwachitsanzo muyenera kudziwa zina za malamulo Achiroma kuti mumvetsetse chifukwa chenicheni chachiphunzitsochi. Malamulowa anapangidwa pofuna kuphunzitsa mwini banja wa Chikhristu za m’mene angasamalire banja lake. Miyambo ya nthawi imeneyo inkalangiza abambo kuti akazi awo azikhala omvera komatu sankalimbikitsa chikondi ngati udindonso wa abambo. Paulo m’buku la Aefeso 5:25-31, akuphunzitsa kuti bambo wa chikhristu ali ndi udindo woteteza ndi kukonda mkazi wake.
C. M’mene nkhani za malonda ndi chuma chimayendera zingakuthandizeninso pakuwerenga kwanu. Makamaka tikamvetsa za m’mene umphawi unaliri pa anthu wamba nthawi imeneyo tikhoza ndithu kudziwa za udindo wathu opereka moolowa manja ku mpingo. Onani 1 Mbiri 29 ndi 2 Akolinto 8 pomwe tikuphunzira kuti anthu osauka pa nthawiyo ankapereka moolowa manja chomwe chiri chitsanzo kwa ife lero lino.

D. Zimathandiza kudziwa malamulo anthawi imeneyo. Timawerenga m’buku la Machitidwe 16:37-39 kuti Paulo monga mzika ya Chiroma anali ndi maufulu ena. Malamulo amenewa anampangitsa iye kuti asakwapulidwe ndipo analoredwa kupereka dandaulo (Apilu) kwa Kaisara kuti akazengedwe mlandu ku Romu.
E. Kudziwa zinthu ngati izi zimatithandizira kumvetsetsa Baibulo bwino. Chitsanzo ngati ichi chimapezeka m’buku la Masalimo lomwe liri Salimo lalikuru la chitonthozo. Tikudziwa kuti m’busa anasamala nkhosa zake apa tikuona kuti Mulungu amasala anthu ake. Amatitsogolera ndi kutiyang’anira. Palibe chifukwa chochitira mantha chifukwa tiri ndi m’busa wabwino Yesu Khristu yemwe amatisamalira.

IV. Tanthauzo ndi phunziro

1. Kodi mlembi watsimikiza za tanthauzo la ndimeyo? Anthu ena amaganiza kuti amene akuwerenga ndi amene akhoza kupeza tanthauzo. Koma ngati mumakhulupilira kuti Mulungu ndiye mlembi wa Baibulo ndipo analemba kuti akuphunzitseni choncho muyenera kuwerenga Baibulo kuti mupeze tanthauzo lomwe Mulungu akufuna kuyankhula.

A. Limodzi la malamulo lokhudza kumasulira ndi kutanthauzira Baibulo ndikusadzipatsa tokha tanthauzo. Komatu tiyenera kupeza tanthauzo lomwe ndimeyo ikufotokoza lolembedwa ndi mlembi. Cholinga chathu ndi kupeza tanthauzo lomwe Mulungu analipereka kwa ife.

2. Tiyenera kufotokozera tanthauzo ndi phunziro.

A. Tanthauzo ndi limene wolemba ankafuna kufotokoza pamene ankalemba ndimeyo. Tanthauzo limafotokozedwa ndi mlembi wa Baibulo.

i. Chitsanzo ndi malangizo a Mulungu a m'mene tingafikire kwa Iye. Tikhoza kufika kwa Mulungu kupyolera mwa Yesu Khristu yekha. Izi ndi zomwe mlembi ankafuna kufotokoza (Yohani 14:6).

ii. Anthu ena akawerenga amaganiza ndi kukhulupilira kuti owerenga akhoza kupereka tanthauzo m'mene iyeyo akufunira. Anthu ena ndi mipingo ina amapereka matanthauzo awo pa buku la Yohani 14:6. Amati Mulungu wao ndi wankuru kuposa m'mene Baibulo likufotokozera ndipo Mulungu adzapulumutsa anthu onse amakhalidwe abwino monganso Asilamu. Koma iri ndi bodza ndi nkulakwitsa kwakukuru.

B. Phunziro ndi limene munthu amapereka lochokera pandime yolalikidwayo. Zomwe tikhoza kuchita pa chitsanzo chomwe chiri pamwamba monga Yohani 14:6 ndi kutsimikiza kuti tiri ndi Yesu monga Mbuye wathu kapena kulephera apo sitidzapita kumwamba.

3. Kupereka tanthauzo

i. Musayerekeze kuchita masewera ndi mau a Mulungu pokhapokha ngati mukudziwa chomwe Baibulo likutanthauza. Mukhoza kudziwa chomwe Baibulo likutanthauza koma osafuna kugwiritsa ntchito zomwe mwaphunzirazo; ukunso nkulakwitsa. Kungodziwa kokha zomwe Baibulo likufuna nkopanda pake koma muyenera kuchita zomwe Baibulo likufuna kuti inu muchite.

i. Chitsanzo chabwino gawo lofalitsa uthenga wabwino (Mateyu 28:18-20). Likanakhala kuti lamulo limeneli limatsatiridwa mokhulupirika, dziko lonse lapansi likanalandira uthenga wa Mulungu pamene nthawi yatha tsopano zaka zikwi ziwiri, komatu mpaka pano anthu ambiri sakudziwabe choonadi cha Yesu Khristu. Ku dziko la America kuli zikwi zikwi za anthu ophunzira bwino za uzimu omwe akanatha kukhala kumadera onse a padziko lapansi monga abusa opanda dera (mamishonale) komatu amakonda kukhala komweko posangalala ndi moyo wawo.

V. Kumvetsetsa magawo ambiri a Baibulo

1. Chipangano Chakale

A. Pali njira zisanu zomasulira Chipangano Chakale. Njira zonsezi sizigwira ntchito pandime zonse za Baibulo.

i. Njira yoyamba ndikupeza tanthauzo lenileni la chomwe wolemba ankafuna kwa anthu omwe iye ankawalalikira.

ii. Njira ya chiwiri kupeza kusiyana kwa anthu Chipangano Chakale ndi ife lero lino.
iii. Njira yachitatu kupeza mfundo yeniyeni ya ndime yolakidwa.
iv. Njira yachinayi kupeza m'mene Chipangano Chatsopano chikufotokozera mfundo. Mwachitsanzo kudya nkhumba.
v. Njira ya chisanu kupeza m'mene tikutanthauzira zimene zikuwerengedwazo lero lino.

B. Lamulo kapena mabuku asanu oyambilira a Baibulo (Genesis, Exsodo, Numeri, Levitiko ndi Detronomo)

i. Lamulo likuperekedwa ngati gawo la mbiri ya ana a Israeli.
ii. Lamulo likuperekedwa ngati pangano lazochitika lotchedwa Pangano la Mose.

Exsodo 19:24

iii. Tiyeni timasulire Lamulo la Mose:

a. Madalitso a Mulungu ankadalira kumvera kwa ana a Israeli.
b. Tsopano sitiri pansi pa lamulo la Mose chifukwa panakhazikitsidwa Pangano la Tsopano.

Pangano la Tsopano

c. Chiphunzitso cha Chipangano Chatsopano chikuti pamene ife sitiri pansi pa Chipangano Chakale, komabe pali zinthu zambiri zofunikira ndi maphunziro ena zomwe ziyenera kutsatidwa makamaka tikaziyang'ana kupyolera m'Chipangano Chatsopano.
d. Pamene tikuwerenga Chipangano Chatsopano tikuona kuti sitiyenera kutsatira malamulo ansembe komatu Malamulo Khumi tiyenera kuwatsatirabe. Kotero kuti tikhoza kudya nkhumba koma tiyenera kumvera Malamulo Khumi.

C. Maulosi a Chipangano Chakale ndi osavuta kuwamva komanso nthawi zina amavutanso kumvetsetsa.

i. Poyamba tiyenera kudziwa ngati wolembayo anagwiritsa ntchito mau osavuta; lamulo iri liyenera kuchitika pa mau onse a m'Baibulo. Werengani ndime ndipo onetsetsani ngati liribe tanthauzo lina la padera pokhapokha ngati pali chitsimikizo choti mauwo ndi chining'a (chizimbaitso).
ii. M'mene timamasulira ndime zozimbaitsidwa; poyamba tiyenera kupeza mau omwe akhoza kupereka tanthauzo losavuta. Ndipo ngati palibe masulirani mwachining'anso mwachitsanzo Yesaya 55:12 "tikaonatu ndimeyi mapiri sangaimbe ndipo mitengo singaimbe m'manja. Chinthunzi chomwe wolemba akufuna kusonyeza ndi chimwemwe chopambana."
iii. Tiyenera kufufuza ndi kuonetsetsa pa zolembadwa za aneneri pomasulira mwa dongosolo.

a. Kawirikawiri uthenga wa aneneri unkadzudzura kusamvera kwa anthu ndi chilango chomwe anthu osamvera ayenera kulandira. Nthawi zonse aneneri ankapempha anthu kuti alape ndipo akatero ankakhulurukidwa, komabe nthawi zina Mulungu sankawalekerera ndipo ankalangidwa.

b. Aneneri ena ankalosera za m'tsogolo. Nthawi yino ndi maulosi ochepa okha amene sanakwaniritsidwe omwe analoseredwa ndi iwo. Maulosi ambiri anakwaniritsidwa.

i. Tiyenera kudziwa mbiri ndi chomwe chinkachitika pa nthawi ya wolembayo. Kodi m'neneri ankalalikira ndani?
ii. Uthenga weniweni unali kupita kwa anthu a nthawi imeneyo. M'neneri kwake kunali kuchenjeza kuti anthu anali kuchimwa ndipo Mulungu awalanga iwo pokhapokha atalapa kwa Mulungu ndi kubwelera ku zochimwa zawo. Ichi chimatchedwa chiphunzitso.

D. Ndakatulo Za Chiheberi (Chiyuda) – Mabuku a Yobu, Masalimo, Miyambo, Mlaliki ndi Nyimbo ya Solomo.

Gawo lalikuru la Chipangano Chakale linalembedwa monga ndakatulo choncho nkofunikira kwambiri kwa omasulira Baibulo ndi alaliki kudziwa m'mene ndakatulo za Chiheberi zimakhalira. Kawirikawiri ndakatulo za Chiheberi ziri ndi chizolowezi chobwereza chinthu chimodzi kawiri. Chibwereza chakhala chiripobe osasokonezeka mpaka lero lino. Kotero chibwereza chimenechi chakhala chikugwiritsidwa ntchito m'ziyankhulo zonse popanda kusokonezeka mwa njira ina iriyonse.

i. Magawo a ndakatulo
   a. Chibwereza chimakhudza maganizo ofanana ndipo chimakhala chosiyanasiyana onani Masalimo 3:1-2 machitsanzo.
   b. Maganizo amene akuperekedwawo ndi ofanana (Masalimo 25:4).
   c. Chiganizo chachiwiri chimamalizidwa ndi choyamba (Masalimo 23:1)
   d. Chiganizo chachiwiri chimalekana ndi chiganizo choyamba (Masalimo 1:6)
ii. Alakatuli ankalemba pofuna kuika chithunzithunzi m'maganizo mwa owerenga popereka zinthu zopenyeka ndi maso zomwe zimakwaniritsidwa m'zining'a
   a. Chining'a ndi kulankhula mozimbaitsa. Mau amagwiritsidwa ntchito mokuluwika. Mau enieni amagwiritsidwa ntchito mwa njira zina.
   Mwachitsanzo:

"Ndinam'menya ndi ndodo" - tanthauzo lenileni "kumenyedwa ndi ndodo."
"Ndinam'menya ndi mawu" – 'tanthauzo la chining'a kukalipiridwa, kunyozedwa etc.

Timagwiritsa ntchito zining'a pofuna kufanizitsa mosagwiritsa ntchito mau monga "ngati" chifukwa tikatero imakhala nthabwala (tchedzero). Nthabwala kuyerekeza kapena kufanizitsa zinthu ziwiri mwachitsanzo "Anabanda ali ngati mwana." Pamene nthabwala imafanizitsa kapena kuyerekeza 'zinthu ziwiri chining'a kapena nkuluwiko umatsimikiza kuti chinthucho ndi chomwecho basi.

Pamene nthabwala imafotokoza kuti chinthu china ndi chofanana ndi china, chining'a chimanena kuti chinthu chinacho ndi chomwecho basi. Pamene nthabwala ikuti "matupi athu ali ngati udzu" (Petro 1:24), mkuluwiko umanena molunjika kuti "matupi athu ndi

udzu" (Yesaya 40:6) Uku ndi kusiyana kwa nthabwala ndi chining'a. Nthabwala ikuti "Tonse tiri ngati nkhosa;" mkuluwiko umati "ndife nkhosa za pabusa."

b. Kukokomeza: kufotokoza mau mokweza kapena mokulitsa pofuna kutsimikiza (Masalimo 6:6)

Njira zomasulira ndakatulo za Chiheberi:

Masulirani poyang'anira chomwe chikuchitika. Yang'anitsitsani zinthu zomwe zikuthandizira kugawa masalimo mpaka pa malekezero pa chiganizo. Onani mizere ya ndakatulo yomwe ikupanga gawo la chiganizo pofuna kutsimikizira kufanana pamene mau ofanana akugwiritsidwa ntchito.

2. Kumasulira Chipangano Chatsopano

A. Mafanizo

Munthu amene amadziwa kufotokoza bwino nkhani amakhala ndi gulu lomwe limamumvetsera. Yesu ankadziwa kufotokoza nkhani bwino; ndipo nkhani zake zinali kuphunzitsa zauzimu ndi zina zanzeru. Nkhanizi zimatchedwa Mafanizo. Pafupifupi theka la zomwe Yesu anaphunzitsa zomwe zikupezeka mu Uthenga Wabwino ziri m'mafanizo chifukwa anali kunena mafanizo nthawi zambiri (Mateyu 13:34). Nthawi zonse anthu amakumbukira nkhani zabwino.

Fanizo ndi nkhani yomwe imafotokozedwa kuti iphunzitse chinthu choonadi kapena pofuna kuyankha funso. Pamene Yesu anali kuphunzitsa m'mafanizo anali ndi cholinga chapadera. Ankafotokoza ndi cholinga chofuna kubisa choonadi kwa anthu amene sankafuna kulandira uthenga wake, ndikufotokozera bwino momveka kwa amene ankalandira uthengawo. Njira ina yomwe tingafotokozere izi ndi kupereka tanthauzo lenileni la fanizo ku mpingo. Tikhoza kuchita izi pogwiritsa ntchito zinthu zochitika m'moyo wathu nthawi zonse zomwe zikhoza kumveka bwino.

Mafanizo makamaka amayerekeza nkhani yochitika ndi Ufumu wa Mulungu pakutero timaphunzira chinthucho.

Njira zinayi zomwe tingamvetsetsere mafanizo:

1. Yambani ndi chomwe chikutanthauzidwa. Kodi mutu weni weni wa nkhaniyi ndi otani?

A. Luka 15 timadziwa kuti ndi fanizo la mwana olowelera. Kodi mutu waukulu wa nkhaniyi ndi uti? Yesu anafotokoza za nkhaniyi pofuna kuonetsa kusiyana kwa kusakhululuka kwa mwana wamkulu ndi kukhululuka kwa Atate yemwe akuyimira Yesu Khristu.

B. Nthawi zina tanthauzo la fanizo limaperekedwa pofuna kuphunzitsa monga Mateyu 24:44. Apa tanthauzo ndi: tiyenera kukhala okonzeka kuti Yesu akhoza kufika nthawi iriyonse.

2. Pezani mfundo zomwe sizikugwirizana. Fanizo la Luka 17:7-10 liri ndi magawo ambiri omwe siofunika pa choonadi kuchiphunzitso chomwe chikuphunzitsidwacho. Chinthu chopambana choti mudziwe ife sindife opambana podziwa zinthu zolondorazo.
3. Pezani zomwe zikugwirizana.

A. Atate akuthamanga kukumana ndi mwana m'nkhani ya mwana olowelera ndi yogwirizana. Kuthamanga kwao kukusonyeza mtima wao kuti anali kudikilira mwana wawo. Izi ndi zinthu zogwirizana.

4. Mfundo zina zomasulira mafanizo

A. Kawirikawiri fanizo limakhala ndi phunziro limodzi lofunika kwambiri.
B. Nthawi zina phunziro limapezeka pachiyambi cha fanizo mwachitsanzo Luka 18:3-10.
C. Nthawi zina cholinga cha fanizo chimabvumbulutsidwa kumapeto; onani Luka 15:3-10.
D. Musapereke tanthauzo lanu pa chirichonse chikunenedwa m'fanizo.Chifukwa simuyenera kupeka matanthauzo omwe olankhulayo sananene.
E. Sitiyenera kukhazikitsa phunziro lina lirilonse pa fanizo. Simuyenera kutenga magawo ena a fanizo kukhala maziko a chimene mukuphunzitsa. Fanizo likhoza kutsogolera ku phunziro; komatu ziphunzitso zonse ziyenera kuchokera ku ndime zomveka bwino. Mwachitsanzo Mateyu 25, ndime yomwe ikufotokoza za anamwali asanu opusa, palibe chiphunzitso chirichonse pamenepa. Tikuphunzira kuti tiyenera kukhala okonzeka nthawi zonse pa zakubwera kwa Khristu. Phunziro lomwe likuphunzitsa zimenezi timalipeza m'ndime zomveka bwino m'magawo ena a Baibulo monga Machitidwe 1:11, Yohani 14:3 and Chibvumbulutso 1:7.

VI. Mathero a phunziro lathu

1. Baibulo lonse komanso ziphunzitso zake zonse zikuruzikuru ziyenera kuwerengedwa komanso kuzimvetsetsa monga zinalembedwera. Ziphunzitso zomse zazikuru zomwe ziri m'Baibulo ndi zomveka bwino ndipo zimabwerezedwa kawirikawiri kuti tisalephere kumvetsetsa ndimezo.
2. Gwiritsani mzeru kumvetsetsa ndime zina za Baibulo

A. Magawo ambiri a Baibulo amathandizana pa zomwe zikupezeka m'ndime zina mpaka uthengawo umamveka bwino pamapeto pake. Izi zimakhala zopitilira ndipo ndime zina zimathandizira kumvetsa kwa ndime zinanso. Kuti tifike pa mathero owerenga amayembekezedwa kugwiritsa ntchito njira zonse zomwe takambirana kale.

i. Tiyeni tione Akolose 1:21-23 ngati chitsanzo cha magawo opezeka:

a. Akolose ataika chifukwa cha tchimo.
b. Apulumutsidwa chifukwa cha imfa ya Khristu.
c. Mulungu akuwayang'ana iwo ngati anthu woyera chifukwa cha ntchito ya Khristu.

3. Kodi mamasulidwe anga akugwirizana ndi Mau a Mulungu? Mamasulidwe anu afanane ndi ndime zina za Baibulo chifukwa Mau a Mulungu sadzitsutsa okha. Gwiritsani Mau a Mulungu kumasulira Mau a Mulungu. Pali m'gwirizano wa Mau a Mulungu. Pamene owerenga wafika pamathero kuti Baibulo likudzitsutsa lokha, dziwani kuti Baibulo liribe vuto lirilonse koma owerengayo. Gwiritsani ntchito magawo a Baibulo omwe akufanana kuti akuthandizeni kumasulira Baibulo.

4. Kodi mamasulidwe anu akugwirizana ndi mamasulidwe anzanu ena? Anthu amakhoza kulakwitsa, komabe fufuzani zomwe anthu ena akuganiza za tanthauzo la ndimeyo musapange chiganizo kuti alakwitsa ndipo inu ndi olondora. Ndi mzeru kumvetsera maganizo akhristu okhazikika kuti akuthandizeni ngati patakhala kusamvetsetsana.

5. Werengani Baibulo mokonzeka kuti muphunzire ndikusintha mtima wanu. Musangofikira pa ndime ndi mtima oti mukuidziwa bwino zomwe zikutanthauza ndipo simungaganizirenso chomwe Baibulo likukamba.

A. Mwachitsanzo anthu ena amaganizira kuti ngati munthu wina atapita kumpingo wina ndekuti iyeyo basi adzapita ku Gehena ndipo sadzapitanso Kumwamba. Akuiwala kuti Yesu adzaweruza anthu aliyense payekha payekha osati gulu la anthu.
B. Yesu anadzudzura mpingo wa Sardis Chibvumbulutso 3. Koma mumavesi 4 -5 akuti alipo ake ochepa mu mpingowo. Iziti zikutanthauza kuti mukhoza kupezeka gulu lochepa la akhristu mu mpingo ulionse. Anthu amene safuna kukhulupilira izi sayeneranso kukhulupilira mavesi amenewa.

6. Thandizo lalikulu lomwe mukhoza kupeza pomasulira Baibulo ndi Mzimu Woyera. Pempherani kuti Mulungu akuthandizeni. Zaka za m'mbuyomu pamene munthu wina wotchedwa Bob anayamba kuphunzitsa Baibulo, Bob anayamba ndi buku la Yesaya. Nthawi zambiri Bob sankamvetsetsa ndime zina ndipo pafupifipu anafuna kusiya. Bob anapemphera kwa Mulungu kuti apeze thandizo lake kenaka anayamba kumvetsa bwino zomwe Baibulo limanena (1 Akolinto 2:14).

7. Machaputala ndi mavesi sigawo la mau oyambilira eni eni a Mulungu. Anthu ndi amene anapanga zimenezi kuti anthu azitha kupeza malo m'Baibulo mosavuta. Nthawi zina ndime imapitilira kupyora mu chaputala china. Koma musalole kuti chaputalacho kapena vesilo likupangitseni kusamvetsetsa ndimeyi.

8. Musamangoyang'ana chiphunzitso chanu pa vesi limodzi lokha. Ziphunzitso zoti chikhulupiliro ndichochipulumutsa osati ntchito zimaphunzitsidwa m'Baibulo lonse – onani Yohani 3:27; 6:52-65; Afilipi 1:29, Machitidwe 18:27; Aefeso 2:8-10, ndi zina.

A. Nthawi zambiri anthu amagwiritsa molakwika vesi pofuna kulungamitsa zomwe iwo akuchita. Mwachitsanzo:
i. Mateyu 19:12 chimagwiritsidwa ndi mipingo ina kuti m'busa sayenera kukwatira. Uku sikumasulira molondora Baibulo.
ii. Magulu ambiri akhala akumasulira molakwika Genesis 9:20-27 kulungamitsa zoti anthu akuda ndi akapolo, izinso m'zimene boma la Apafaedi la South Africa linkagwiritsa ntchito kulungamitsa tsankho; anthu ena amanenanso kuti chizindikiro chimene anaika pa Kanani chinali chikopa chakuda, komatu zonsenzi nzolakwika.

VII. Maganizo olondora. Ngati muli ndi Baibulo lomwe liri ndi mamasulidwe pansi pake yang'anani chimene chikutanthauzidwa kapenanso Konkodase, yang'anani tanthauzo la mauwo. Mabaibulo ena amakhala ndi mboni zake pakati, yang'ani mbonizi. Yang'anani Konkodase wanu pomwe mauwo akupezeka m'Baibulo.

VIII. Chiganizo chomaliza pakumasulira Baibulo ndi kupeza thandizo lochokera kwa Mulungu mwini wolemba. Pempherani ndipo pemphani kwa Mulungu kuti akuthandizeni kumvetsetsa ndime yomwe mwasankhayo. Pamene mukuvutika kumvetsetsa tanthauzo, nthawi zambiri tanthauzo limabisika. Yesetsani kuti mumvetsetse zomwe Mulungu akunena. Ngati simukumvetsabe, siyani, ndipo pempherani ndipo pemphani Mzimu Woyera kuti akuthandizeni kumvetsetsa tanthauzo lake ndipo Mulungu adzakuthandizani.